**ttb_Nya_0835_script**

**2 Atesalonika :1:1-3**

**Mutu : Mau Oyamba**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyeni Ambuye atitsogolere ndi mau apaAhebri 4:16, pamene pali mau akuti, "Potero tirimbike mtima poyandikira mpando wachifumu wachisomo cha kutithandiza nthawi yakusowa."

Mupologalamu yatha tinali kusanthula 1 Atesalonika 5:11-28, m'mene timaona za malamulo ya akristu. Ndipo lero pamene tikulowa mu 2 Atesalonika 1:1-3, tikambirana za mau oyamba.

Kalatayachiwiri ya Atesalonika idalembedwamotsatana ndi yoyamba pakati pa chaka cha 52 ndi 53 AD.

Akhristu aku Atesalonika anali makanda mu mzimu pamene Paulo amawalemberakalatayi.Iwo, atawerengakalata yoyamba adali ndi mafunsoenanso amene adapangitsa kuti awalemberekalatainapoyankhamafunsowo. Pakati pawo padalikalatainayachinyengo imene sinachokere kwa Paulo.

Kalatayachinyengoyoidalembedwandicholinga chofuna kungosokonezaakhristu.Kalata imeneyi imanena kuti Yesu Khristuadabwera kale ndipo adatenga kale mpingo wake kotero kuti mpingo udaliutalowam'chiweruzo cha Tsiku la Ambuye. Ndiye akhristu awa amazunzidwa monga tidawonam'kalata yoyamba ija.Amazunzidwa chifukwa cha Uthenga Wabwino kotero kuti kunali kosabvuta kuti akhulupirire kuti adali atalowa m'nyengo ya Chizunzo Chachikulu.Kukadakhalakosabvuta kukhulupirira kuti akhristu onse amoyo ndi akufa,adasiyidwa pa tsiku la mkwatulo. Paulo akutsutsandikuthetsa nkhawa zimenezi m'kalatayachiwiriyipofotokoza kuti nyengo ya mkwatulosinafike ndipo pali zinthu zomwe ziyenera kuchitika nthawi imeneyi isanakwane (2 Atesalonika 2:1). Zina mwa zinthu zomwe ziyenera kuchitika ndi monga kuzimakwa chikhulupiriro cha uzimu ndi kudza kwa "munthu wa uchimo."

Paulo akunena kuti chikhulupiliro cha anthu mumpingo chidzazima,Chizunzo Chachikulu chisanafike.Iyi, ndi nkhani yomwe Ambuye pa Luka 18:8 adafunsa kuti;"Koma mwana wa munthu pakudza Iye, adzapeza chikhulupiriro pa dziko lapansi

kodi?”yankho likuti, ayi ndithu.  Ambuye sadzapezachikhulupiriro pa dziko lapansi pamene adzabweranso.Mpingo udzakhalautataya chikhulupiriro kotheratu.Izi zimatsimikidwa m’buku la Chibvumbulutso 4, momwe mpingo wachoka pa dziko lapansi ndipo chimene chatsala ndi gulu la anthu osonkhana ngati mpingo okhala ndi mawonekedwe a chipembedzo koma okana mphamvu ya Mulungu.Mpingo wakufa otere ndi womwenso uli pa Chibvumbulutso 17,pamene timapeza chithunzi chochititsa mantha kwambiri m’Mau a Mulungu.

Kalata yoyamba ya Atesalonika imafotokoza za mkwatulo koma kalatayachiwiriimalongosolazakubweransokwachiwirikwa Ambuye Yesu kudzakhazikitsa ufumu wake. Ichi ndi Chibvumbulutso.Monga tidawonam’kalata yoyamba ija Ambuye adzakwatula mpingo mosafika padziko.Anthu okhulupiriraadzakumana ndi Ambuye mu mlengalenga (1 Atesalonika 4:17).Kukwatulidwakumatanthauzakusompholedwamonyamulidwa ndi mphamvu.Mpingo udzakwatulidwa kukakumana ndi Ambuye mu mlengalenga.Koma kalatayachiwiriikubvumbulutsa zimene zidzachitike pamene Ambuye adzabwere kudzakhazikitsa ufumu

wake.Nthawi yapakati pazinthuziwirizi padzakhala nyengo ya Chizunzo Chachikulu.

Monga tidawonam'kalata yoyamba, mkwatulo ndi nkhani imene timayipeza m'Chipangano Chatsopano.M'Chipangano Chakale sitiwerenga za mkwatulo.Okhulupirira m'Chipangano Chakale amadikira Mpulumutsi Wolonjezedwa amene kwa iwo amaganiza kuti adzakhazikitsa ufumu wake padziko lapansi. Koma ufumu umene amaphunzitsa Ambuye Yesu ndi ulamuliro waMulungu, ndiumene amanena kuti ufumu wakumwambawayandikira.

Tsono kalatayi tikhoza kuyigawam'mituitatu motere:

**I. Mazunzo ya Khristu Masiku ano; Chiweruzo cha anthu osakhulupiriraPobwera Yesu 1:1-12**

A. Mau Oyamba 1:1-2

B. Mazunzo a Khristu ndi Zotsatira Zake 1:3-7

C. Chiweruzo cha Ochimwa Pobwera Ambuye 1:8-12

**II. Ndondomeko ya zochitika pa Dziko pobwera Ambuye 2:1-12**

A. Mkwatuloudzachitikapoyamba 2:1

B. Tsiku La Ambuye, Kuzima Kwa Chikhulupiriro ndi Munthu wa Uchimo 2:2-5

C. Kukhala Mosaweruzidwa Masiku ano, WosaweruzidwaAmangidwa ndi Mzimu Woyera 2:6-8

D. Wosaweruzidwa pa Tsiku La Chizunzo Chachikulu 2:9-12

**III. Zoyenerapodikirakubwera kwa Ambuye 2:13-3:18**

A. Okhulupiriraakhazikike M'mau 2:13-17

B. OkhulupiriraakhazikikeM'mayendedwe 3:1-7

C. OkhulupiriraakhazikikeM'ntchito 3:8-18

Tiyeni tsopano tiyambe kusanthula 2 Atesalonika 1:1-2;

1. Paulo, ndi Silvano, ndi Timoteo, kwa Mpingo wa Atesalonika mwa Mulungu Atate wathu ndi Ambuye Yesu Khristu

Paulo akulonjera mpingo monga amachitira m'makalata ake.Popereka moni Paulo akutchula mainaa atumiki anzake Silvano ndi Timoteo kusonyeza kudzichepetsa. Silvano ndi dzina la Sila mwachidule.Atumiki atatu awa adazunzidwa kwambiri chifukwa cha Uthenga Wabwino.Paulo ndi Sila anali m'ndende ku Afilipi.Paulo, Silvano ndi Timoteo adapita limodzi ku Atesalonika komwe Paulo adawasiya awiriwa atathamangitsidwa.Adakawadikira

ku Atene koma adapitirira yekha kupita ku Korinto chifukwa anali asanakumane ndi Silvano ndi Timoteo ndipoadakakumanso ku Korinto.Ndiye kunali ku Korinto kumene Paulo adalembakalata yoyamba yopita ku Atesalonika kuyankhamafunso amene okhulupirira aku Atesalonika adali nawo atachokakumeneko.

Polembakalatayachiwiri, Paulo akutchukansomainaa atumiki anzake amene anali ngati abale ake.  Anthu awiri amenewa sakadadziwikampang'ono pomwe masiku ano akadakhala kuti Paulosanawatchulem'makalata ake.Apatikuwona kuti Paulo adali mtumiki osadzikonda.  Kumbukirani kuti Paulo adalimfarisi wonyada ndithu koma tsopano adatembenuka kukhala mtumiki wa Ambuye Yesu Khristu wodzichepetsa.  Pano Paulo ndi kapolo wa Ambuye komanso mtumiki wake.

Pamene Paulo akunena kuti, “Kwa Mpingo wa Atesalonika.” akutanthauza mpingo umene umakumana ku Atesalonika.Iye, amazindikira mpingo potchula kumene umasonkhana.Mpingo umenewu umakumana ku Atesalonika koma unali wokhazikika “mwa Mulungu Atate wathu ndi mwa Ambuye wathu Yesu

Khristu."Mzimu Woyera amakhala mwa okhulupirira onse mu mpingo umenewu.Mzimu Woyera adawapatsakuthekerakowonetsa moyo watsopano mwa Yesu Khristu ndi makhalidwe olongosoka monga mwa mayitanidwe mwa Mulungu Atate.Akhristu aku Atesalonika anali mwa Mulungu Atate wathu ndi Yesu Khristu Ambuye wathu.Kwa mtumwi Paulo Yesu anali Mulungu Mwana mopandachikayiko chirichonse. Taonani pa Yohane 10:27-29 Yesu akunena kuti: Nkhosa zanga zimvamawu anga, ndipo Ine ndizizindikira izo, ndipo zinditsata Ine. Ndipo Ine,ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzawonongekakunthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m'dzanja langa. Atate wanga, amene adandipatsa izo aliwamkulu ndi onse; ndipo palibe wina angathekuzikwatula m'dzanja la Atate."

Wokondedwa anzanga apaulendo, pa vesiloyamba la kalatayitikuwona dzanja la Mulungu Atate ndi la Mulungu Mwana.kutsimikiza kuti Mpingo uli m'dzanja la Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana. Mpingo wa Atesalonika unali m'dzanja la Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana. Kodi inu mpingo wanu uli m'dzanja la ndani?Tamvetsani wokondedwa, kuti chinthu chofunika sidzina la mpingo wanu ayi, koma chinthu chofunika

kudziwa ndikutimpingo wanu uli m'dzanja mwa ndani?Kodi uli m'dzanja mwa Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana?Chimenechondiye chofunika kwambiri.Mzimu Woyera amakhala pakati pa mpingo otere ndipo mphamvu yake imawoneka kudera kumene kuli mpingowo, m'dziko komanso mbiri yake imadziwika padziko lonse lapansi. Mpingo umene uli m'manja mwa Mulungu Atate ndi Mulungu Mwana umawonetsera moyo wa Mulungu pa dziko lapansi. Chimenechi ndichimene akunena Paulo pamalonje ake m'kalatayi.

2. Chisomo kwa inu ndi mtendere wa kwa Mulungu Atate ndi Ambuye Yesu Khristu.

Chisomo ndi mtendere ndi mau ofunika kwambiri mu Uthenga Wabwino. Chisomo chimabweretsa mtendere kutanthauza kuti chinthu chimene chimayambapam'ndandawa chipulumutso ndi chisomo. Ngati mudalandira chisomo cha Mulungu ndiye kuti ndinu opulumutsidwa.Tamvani mau apaAefeso 2:8-9, akuti, "Pakuti muli wopulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu; chiri mphatso ya Mulungu: Chosachokera ku ntchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense."Kunena kuti timalandira chisomo tikadziperekakwa

Mulungu mozindikira kuti ndife otayikam'machimo athu, ndipo kuti tilibe kalikonse kotiyenenereza pamaso pa Mulungu ndikulandira zonse kwa Mulungu. Pamenepo Mulungu amatipatsa chisomo chake.Mphatso ya ulere ya Mulungu ndi moyo wosatha mwa Khristu Yesu Ambuye wathu. Mphatso imaperekedwakwaulere. Kutsindika kunena kuti ngati mwachita china chake kuti mulandire kanthu sitinganene kuti mwalandirayo ndi mphatso ayi.Ngati munagwira ntchito kuti mulandire china chake ndiye kuti mwalandira malipiro kapena mphoto. Chipulumutso sichinthu chimene chimaperekedwakwa anthu amene achita bwino m'moyo uno; kapena kuti amapita ku tchalitchi sabata iliyonse, kapena kwa ana akonda Sunday school. Pakuti tonse tinachimwa ndipo tinaperewera pa ulemelerowa Mulungu. Palibe amene akuyenerakupulumuka. Mphatso ya chipulumutso sichinthu chimene inu ndi ine, tiyenera kulandira kwaMulungu ayi, koma tiyenera kulandira chilango cha imfa. Ndiye nkhani ikuti Mulungu amapereka mphatso ya chipulumutso kwa anthu ochimwa amene amayenera kulandira chilango cha imfa,pameneakhulupirira Iye mwa Yesu Khristu. Chimenechi ndiye chisomo.

“Mtendere” ndi chinthu chimene chimabwerakwa anthu amene alandira chisomo cha Mulungu.  Mtendere umafika chifukwa tsopano machimo ako onse akhululukidwa.  Mtendere sichinthu chimene chimapezeka chifukwa mwakumana ndi munthu amene wakupatsaniuphungu wabwino kapena kwadokotala.  Mtendere ndi mphatso ya Mzimu.  Mtendere ndi chinthu chauzimu, umachokera kwa Mulungu Atate ndi kwa Ambuye Yesu Khristu.  Ndiye tikuti ngati mulibe mtenderee mukhoza kukhala nawo chifukwa ndi mphatso imene Mulungu amaperekakwa anthu ochimwa amene akhulupirira Mulungu kudzera mwa Mwana wake Yesu Khristu.

Paulo akupereka moni mwa Mulungu Atate ndi Ambuye Yesu Khristu.Kutanthauza kuti ife ngati ana ake, tiyenera kumulemekeza chifukwa cha chisomo chimene timalandira kwa Mulungu Atate kudzera mwa Mwana wake amene ali Ambuye wathu Yesu Khristu. 1 Petro 5:10, adalemba kuti “Ndipo Mulungu wa chisomo chonse amene adakuyitanani kulowa ulemerero wake wosatha mwa Khristu Yesu, mutamva zowawa kanthawi, adzapanga inu angwiro, adzakhazikitsa, adzalimbikitsa, adzachirikiza inu.”Kutanthauza

kuti inu ndi ine, tidayitanidwa ku ulemelerowa Mulungu ndi Mulungu, wa chisomo chonse. Mtendere umachokera kwa Mulungu Atate kudzera mwa Mwana wake amene ndi Kalonga wa Mtendere. Yesaya 53:5, ananena kuti “chilango chotitengera ife mtendere chinamgwera Iye.”Kutsimikikiza kutiMulungu anapereka mtendere kwa anthu wochimwa mwa mwazi wokhetsedwa pa mtanda wake.

3. Tiziyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu, abale, monga kuyenera, pakuti chikhulupiriro chanu chikulachikulire, ndipo chichulukirachikondano cha inu nonse, yense pa mzakemochuluka.

Mundime iyi, ndi ndime yotsatira, Paulo akukamba za chikhulupiriro, chikondi ndi chipiriro monga adalembansom’kalata yoyamba pa 1 Atesalonika 1:3 pamene anati, “Ndi kukumbukira kosalekeza ntchito yanu ya chikhulupiriro, ndi chikondi chochitachita ndi chipiliro cha chiyembekezo cha Ambuye wathu Yesu Kristu, pamaso pa Mulungu atate wathu.”Mau atatu amenewa akufotokonza zinthu zimene siziwoneka ndi maso koma ntchito zake zimawonekera poyera.Munthu amene wapulumutsidwa mwa chikhulupiriro amawoneka ndi ntchito zake.Chikhulupiriro

chimayamba kuchita ntchito mwa anthu okhulupirira.Chikhulupiriro chimabala chikondi mumtima mwa okhulupirira.Ana a Mulungu amadziwika chifukwa amakhala okondana wina ndi mzake.

Tere Paulo pano, akuyamika Mulungu chifukwa chachikhulupiriro cha Atesalonika chimene chikulachikulire ndi chikondi pakati pawo.Mwanjira ina tikunena kuti paulo akuyamika Mulungu chifukwa chakuti moyo wa atesalonikaumawonekeratu kuti ndi akhristu. Ichi ndi chifukwa chachikulu zedi,chofunikadi kuyamika Mulungu. Anzanga munthu akakhala kuti sakuwonetsa chizindikiro chirichonse chakukula ndiye kuti pali mabvuto pamenepo. Akhristu ambiri komanso mautumikiena, sawonetsa chizindikiro chirochonse chakuti akukula.Komanso kukulamonyentchera ndichizindikiro cha bvuto mwa mkristu kapena utumiki wake. Koma apa tikumva kuti panali kukulachikulire, kutanthauza kuti amapitilirabekukula.

Pachifukwa chimenechi, Paulo akunenetsa kuti, “tiziyamika Mulungu nthawi zonse.” Madalitso onse amachokerakwa Iye, ndipo

amatipatsa chisomo mochulukirachulukira.  Powona chisomo ndi mtendere zimene Mulungu adaperekakwa Atesalonika ndi chikhulupiriro chawo chimene chimakulirakulirabe, Paulo akuyamika Mulungu.  Ndikoyenera kuti atumiki a Mulungu aziyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha chisomo chimene amachitira anthu amene timawatumikira.  Atumiki ayenera kuyamika Mulungu chifukwa anthu amasinthika chifukwa cha ntchito ya Mulungu wa chisomo chonse,m'miyoyo ya anthu osati chifukwa cha ntchito ya atumikiwo ayi.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikuti chikhulupiriro cha Atesalonika chinali chaching'ono ngati kambeukampiruPoyamba, koma tsopano chimawonekachikukulamowirikiza.Pachifukwa cha chikhulupiriro chimene chimakulirakulirabe, Paulo akuyamika Mulungu.Paulo amadziwa kuti inali ntchito ya Mulungu m'moyo mwa Atesalonika kuti apitilizekukula m'chikondi, chikhulupiriro chochitachita mwa chikondi, ndi chiyembekezo chachipiriro.Chifukwa cha izi Paulo amalemekeza Mulungu.

Pa vesilotsatira Paulo akukamba za kupirira m’masautso.Kutanthauza kuti njira yopitaKumwamba sitiyenda ngati pa mseuwamakonowaphula ayi.Kuyenda mwa chikhulupiriro tikhoza kukuyerekeza ndi kuyenda pa mseupamalo pameneukukonzedwa.Pamalo oterewa, inumumachoka pa mseu wabwino,ndikuyenda pa mseuwopatuka umene kawirikawiri umakhala wafumbi komanso wokumbikakumbika kwambiri.Kuyenda kwake kumafunika kupilira.Komabe timayenda pa msewu wotere mopilira chifukwa timadziwa kuti posachedwa tifikanso pa mseu wabwino waphula.Mwina inu mukhoza kukhala kuti mukuyenda pa msewuwopatutsawafumbiwokumbikakumbikapakadali pano.Kutsindika kuti inu simuyenera kutaya mtima ndi zimene mukudutsamo pakali pano.Pilirani chifukwa chachiyembekezo chakuti pakatha mtunda wochepa,muyendansopamsewu wabwino-wabwino.Mwina fumbiladzadza kutsogolo kwanu mwakutisimukuwona kuti posachedwa muchokapamsewuwopatutsawumuyendansopanseu wabwino.Inde mseu wabwino ukhoza kukhala utayandikira kuposa m’mene

mukuganizira.Piliranindikupemba Mulungu kuti akuthangatirenikuyendabepamseu umenewu.

Tsiku ndi tsiku chaka ndi chaka akhristu ayenera kumakulam'chikhulupiriro ndi m'chikondi.Nkhani ikuti inu ndi ine, sitiyenera kulepherakukulapopeza tiyenera kufanana naye Ambuye wathu Yesu Khristu m'chikondi. Kodi inu mukakumana ndi mazunzo mumakhala nacho chipirirochosasuntha chikhulupiriro chanu mwa Mulungu?Kodi mukuchulukirabe m'chikondi cha pa abale?Kodi mukukulabem'chikhulupiriro pokhala moyo wodalira Ambuye muzinthu zonse osaganiziranso zinthu zadziko lapansi kapena zilakolakozathupi?

Tsono Paulo akunena kuti alemekezeke Mulungu chifukwa cha akhristu amene akukula chifukwa tsopano, akukhala mwa chikhulupiriro ndi m'chikondi mwa Ambuye Yesu Khristu.Iye, akulemekeza Mulungu ku Atesalonika chifukwa Mulungu adasintha miyoyo ya akhristu amenewa kudzera muntchito yake yachikondi imene idabereka chikhulupiriro, chikondi ndi chipiriro mwa Atesalonikawomokulirakulirabe.Alemekezeke Mulungu Atate

wa Ambuye wathu Yesu Khristu amene amatiwonetsera chikondi ndi mphamvu yake mochulukirachulukirabe.

Paulo pomalizaakuti ndikoyenera kuti athokoze Mulungu chifukwa cha Atesalonika chifukwa chachikondano cha, yense pa mnzake mochuluka.Kutsimikiza kuti munthu sangakulem'chikhulupirirokomanso m'chikondi cha Mulungu, pamene sakukula m'chikondi cha pa abale. Mulungu amalora kuti nthawi zina tilowem'mazunzo kuti tikule m'moyo wachipiriro. Kutsimikiza kuti masautso ndi gawo limodzi lomwe limathandizira wokhulupirira kukulam'chikhulupiriro.
Kwa lero tilekeza pano. Koma tinali kusanthula 2 Atesalonika 1:1-3, momwe timakambirana za mau oyamba.

Ambuye akudalitseni inu pamene muchilimikam'chikhulupiriro ndi m'chipiliro. Amen!